


KODI MUKUKHULUPIRIRA IZI?

 Ndipo ife tisanapemphere, ine ndikufuna kuti ndinene izi, kuti usiku wathawu, ine ndikukhulupirira unali, ine ndinanena kwa dona, “Ngati iwe utangochita monga mmene talangizidwira kuti tichitire, kuti iwo utero. . .khanda la mutu wa madzi, iwo uphwea.” Ndipo mutu wa khandalo waphwea, usiku wathawu, theka la inchesi pogwiritsa ntchito muyezo wa chingwe. Koteru donayo wachibweretsa icho kuno tsopano.

² Tsopano, chifukwa chimene ine ndinachitira zimenezo, mlongo, ndi kwa cholinga. Mukuona? Ngati iwe utawona chinachake chogwirika chitachitika, chimenecho chingapangitse chikhulupiro chako kuwonjezereka kuti ukhale ukukhulupirabe izo. Nthawizina ine ndimachita zimenezo basi kuti, mwinamwake, monga kumufunsa munthu kuti aimirire, ayende sitepe kapena awiri, kugwedeza dzanja lako, kugwedeza chala chako, basi chinachake chimene iwo angathe kuchita mosiyana, basi kungofuna kuti awone kuti ziri bwino. Iwo amangokhala ndi manjenje ndipo amaganiza kuti sizichitika, koma izo zimachitika nthawi zonse. Mukuona? Izo ziyenera kutero.

³ Ndi angati amene akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero, tsopano? Kodi inu mungakweze manja anu ndi kuti, “Ambuye, perekani izi”? Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

⁴ Ambuye, pamene ife tikumvetsera nyimbo ya mtchalitchi yakale iyi, yolembedwa ndi mzanga wofunika, Paul Rader, “Kungokhulupirira,” ife tikuganizira tsopano za mnyamata, amene anabweretsedwa ndi makolo ake kwa ophunzira, asanathe masiku khumi Yesu atawapatsa iwo mphamvu yotulutsira ziwanda ndi kuchiritsa odwala, ndipo apa iwo anali atagonjetsedwa kwathunthu ndi vuto la khunyu. Ndipo iwo anamuwona Ambuye wathu akubwera. Ndipo bamboyo anathamanga ndipo anati, “Ambuye, mutichitire ife chifundo. Mwana wanga wamwamuna wasautsika ndi mdierekezi. Ine ndinamubweretsa iye kwa ophunzira Anu ndipo alephera kuti amuchize iye.”

⁵ Yesu anati, “Ine ndingathe, ngati inu mutakhulupirira. Mungokhulupirira.” O Mulungu, Inu simunasinthe mpang’ono pomwe chiyambireni nthawi imeneyo: Ndinu yemwe uja wokonda, wokoma, ndi Mulungu wachifundo. Monga Inu munali nthawi imeneyo, chomwechonso Inu muli lero. Ndipo Ambuye, monga bambo uja, ife tonse tikulira, “Ambuye, tithandizeni Inu kusakhulupirira kwathu.” Izo ndi zophweka kwambiri; ife timangopunthwa pa izo, Atate.

⁶ Ife tikufuna kuti tikupatseni Inu mathokozi ndi matamando chifukwa chomukhudza mwana wamng'ono uyo usiku wathawu, kudzawona kuti chigaza icho, chimene chinatupa, kuti icho, kuti fupa latulukira, iwo waphwera ndi theka la inchesi usiku watha. Ndife oyamikira chifukwa cha zimenezo, Atate. Pamene ife tikudziwa kuti madokotala athu alibe chirichonse mofufuzira cha izo, palibe chirichonse chimene iwo angathe kuchita nazo izo; koma Inu mukadali panobe Mulungu, Mwini wa zochitika zonse. Ife tikukuthokozani Inu, Atate. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha kumvera kwa mayi uyu, ndi kukoma, ndi kumvera kuti wabweretsanso chingwecho ndipo wachimata icho pa pepala ili, apa, kuti tisonyeze kwa anthu umboni wake kwa ulemelero wa Mulungu. Mulole khanda lakelo likhale moyo ndipo adzakhale mwana wabwino bwino, kwa ulemelero Wanu.

⁷ Muyang'ane pa mikono yonse iyo imene inakwezedwa mmwamba, Atate. Lirilonse la ilo linali ndi chosowa. Langanso ndakweza, inenso, Atate, ine ndiri nacho chosowa. Ndipo pano pali ambiri pano, mmawonekedwe a kalata kapena mu bokosi ili, amene ali osowa, anthu amene ali osowa kwenikweni. Mulole izo zichitike, Ambuye, kuti aliyense alandire chopempha chake usikuuno. Mulole iwo atenge umboni wa mayi uyu ndipo ngati chitsanzo kukasonyezera kuti pamene Inu munena chirichonse, icho chimakhala kuti chatsirizika. Ndizo . . . Inu . . . Chonse chimene ife tiyenera kuti tichite ndi kulandira izo ndi kuchitapo pa izo. Iyo ndi ntchito yotsirizika.

⁸ Perekani, Ambuye, kuti iliyonse ya makalata awa ndi mipango iyi, anthu amene iyo iti ikaikidwepo, mulole iwo akachiritsidwe. Mmodzi aliyense amene anakweza manja awo, Atate, iwo alandire chokhumba cha mtima wawo. Ife tikupempha izi, mu Dzina la Yesu. Ameni. Inu mukhoza kukhala.

⁹ Ine ndimangofuna kuti ndikusonyezeni inu kachingwe apa, kamene dona. (Ndi kamenekotu. Um-hum.) . . . kuti mutu wa khanda laling'onolo wanyala monga Ambuye anatilonjezera ife kudzera mwa Mzimu Woyera usiku wathawu. Kodi Iye si wodabwitsa? Chotero, zikutipatsa ife chirimbikitso chochuluka kwambiri kuti tikhale ndi chikhulupiriro ndi kukhulupirira.

¹⁰ Tsopano, pamene Yesu ananena kwa mtengo uja, mu Marko 11:23, "Palibe munthu ati adyenso mwa iwe kuyambira pano," Iye mwinamwake sanafuule. Bwanji monga, kunena moona, Iye anazitenga mophweka izo, mpaka ophunzira Ake basi . . . ine ndikuganiza mmodzi wa iwo anamumva Iye. Ndipo izo . . . Pamene wakhunyu uja, pamene iye anabwera pamaso pa Ambuye Yesu, mnyamatayo anali ndi khunyu lovuta kwambiri limene iye anayamba wakhalapo nalo; mwinamwake, anagwa panso ngati kuti wafa, koma iye anazindikira kuti iye anakomana ndi Winawake Yemwe anali ndi chikhulupiriro choposa cha ophunzira aja.

¹¹ Tsopano, ine ndikufuna winawake amene samakhulupirira mu machiritso Auzimu kuti apenye izi. Yesu anali atawapatsa iwo mphamvu yoturutsira mizimu, ndipo iwo anali atalephera. Osati kuti mphamvuyo inali italephera, koma iwowo anali atalephera. Yesu anawauza iwo:

“Chifukwa chiyani ife sitinachitulutse icho?”

Iye anati, “Chifukwa cha kusakhulupirira kwanu.”

¹² Mpingo ukadali nayobe mphamvu. Mulungu sanachotsebe mphamvu Yake kwa mpingo, koma mpingo ulibe chikhulupiriro chokwanira kuti uzichita pa izo. Ndizo zonse. Ndi zophweka chomwecho basi. Ife timayesera kuti tizipange izo zikhale zovuta nthawizina, koma inu mukawupanga Uthenga kukhala wophweka, ndi pamene inu mungakhaleenso ndi zenizeni mochuluka, pamene inu mungakhale mophweka kwenikweni ndi izo: Mulungu ananena chomwecho; izo zikukhazikitsa izo; ndipo ndizo zonse. Ndipo mungokhulupirira izo, nkumapitirira.

¹³ Pamene Yesu anati, “Palibe munthu ati adzadye za iwe,” bwanji, masamba anali okongola basi ndi owala monga amakhalira nthawi zonse. Khungwa limawoneka chimodzimidzi, koma pansi mkati mwa nthaka mmizu imeneyo, moyo unayamba kufota.

¹⁴ Zimakhalanso chimodzimidzi ndi khansa, pa mtundu uliwonse wa nthenda imene—imene inu mungafune kuti muiganizire. Pamene inu mungavomereze Mawu a Mulungu, pansi pomwe kumizu, khansa ikhoza kukhala kuti ili kumeneko; dzanja lanu likhoza kukhala lowuma basi. Zimenezo ziribe chochita chirichonse ndi machiritso Auzimu. Ndizo, “Ngati inu mungakhulupirire.” Mukuona? Pansi pomwe kwina kwake, iyo ndi ntchito yotsirizika kale.

¹⁵ Yesu anati, “Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘Suntha,’ ndipo nkusakaikira mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti zimene mwanenazo zichitika, inu mukhoza kukhala nazo zimene inu mwanena.” Kodi zimenezo si zokoma? Kodi zimenezo zingachokere kwa ndani? Mwana wa Mulungu, Yemwe Mawu Ake . . . Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma tsopano . . . koma Mawu Ake sadzapita.

¹⁶ Tsopano, njira yokhaya imene inu mungachitire izo, inu muyenera kukhala ndi cholinga chabwino ndi chokhumba chabwino. Tsopano, ngati ine nditapita uko ndi kukati, “Ine ndikusonyezani inu kuti ine nditha kusuntha phiri ili, ‘Phiri, suntha.’” Ilo silingasunthe mpang’ono pomwe. Ndithudi ayi. Ziribe kanthu kuti ine ndanena chiyani. Izo ziyenera kukhala . . . Choyamba iwe uyenera kupeza chifuniro cha Mulungu.

¹⁷ Ndi chifukwa chake, kawirikawiri mmizere ya pemphero, ine—ine zimandivuta kwambiri, ndi chifukwa chakuti ndi chinachake chimene chimadutsa mmizere ndi zina zotero, ndipo ndi pamene inu mumapeza izo zikubwerera. Koma taonani,

ngati inu muli ndi tchimo losalapidwa... Kodi inu munayamba mwazindikirapo pa chochitika, ine ndisanafunse mzimu woipa kuti uchoke? Ine ndimayang'ana vuto limenelo motsimikiza kwenikweni kuchitira kuti ndikhale wotsimikiza kuti palibe chirichonse mu moyo umenewo chimene chingatchinge chirichonse, mwaona, chifukwa kumbukirani, pa mphatso izi, iwe ukhoza kulowa nazo mmavuto izo.

¹⁸ Mulungu, inu mukukumbukira nthawi ina, anampatsa mneneri... anampanga mneneri kuchokera mwa munthu, Mose, ndipo anamuza iye kuti apite uko, akalankhule ndi thanthwe. Ndipo mneneriyo anali atatengeka, ndipo anapita kumeneko, ndipo anakalikantha thanthwelo, zimalankhula za kufooka kwa Khristu, kuti Iye adzayenera kuti adzafe nthawi yachiwiri kapena adzakanthidwe nthawi yachiwiri. Iye anali ndi mphamvu yotulutsira iwo, koma icho sichinali chifuniro cha Mulungu.

¹⁹ Ine sindingakhulupirire konse kuti chinali chifuniro cha Mulungu kuti Eliya apite kumeneko, chifukwa ana aja amamuseka iye chifukwa cha dazi lake, ine sindikuganiza kuti iye anayenera kuti achite zimene zija. Koma iye anali mneneri, ndipo anakwiitsidwa, ndipo iye anaika theberero pa ana amenewo ndipo zimbalangondo ziwiri zazikazi zinapha ana aang'ono forte thuu osalakwa awo. Mukuona? Koma ine sindikukhulupirira kuti iye ankayenera kuchita zimenezo. Ndipo izo basi—basi... ife...

²⁰ Mulungu, ine ndikukhulupirira lero, Iye asanawuike mpingo Wake mu mphamvu, Iye amawuyesa mpingo Wake kuti awone chimene iwo uti udzachite.

²¹ Ife... nthawi yotsatira, mwinamwake, ngati Ambuye alola pamene ine ndikamadzabwerera, ife tidzakhala ndi nthawi yoti tidzakhazikike pa chinachake chonga zimenezo, pa chinachake chimene chikukonzekera kuti chichitike, ndiyeno ife tidzadziwa zochulukana za izo pamenepo.

²² Koma ngati inu mutangolankhula mawu, kuti, “Ambuye, ine ndikukhulupirira izo,” osakaikira, kutanthauza izo mu mtima mwanu...

²³ Tsopano, tinene mwachitsanzo, ine ndiri ku chigwa, ndipo ine sindiri... ine ndikulalikira kwa anthu mamillioni, koma basi kutsidya kwa phiriko, kuli gulu la anthu wani handiredi, ndipo iwo akufa osamudziwa Khristu. Chabwino, ine ndiri nawo millioni kuno oti ndiwalalikire, komabe, Chinachake mu mtima mwanga chikundiiza ine, “Pita ukafike kwa anthu amenewo. Ukafike kwa iwo. Iwo akufa.” Ine sindimafuna kuti ndipiteko ndekha, komabe muli Chinachake mwa ine. Mwaona, ameneyo ndi Mulungu zikatero, akuyenda. Mukuona chimene cholingacho chiri, mukuona chomwe chokhumba chopitiracho chiri, osati kwa inemwini... Tsopano, ngati ine nditati, “Chabwino...”

Ngati cholinga changa chiri chabwino chopitira kumeneko, komano ndafika kumeneko ndipo apa pali phiri lalikulu, ine nkuti, “Inu mukudziwa, ngati nditawoloka phiri limenelo ndi kukapulumutsa anthu onse zana amenewo, tsiku lina iwo adzakhala ndi choimikidwa kumeneko: M’bale Branham, wamishonare wamkulu.” Tsopano, cholinga changa si chabwino. Phirilo siligwa. Ayi, bwana.

²⁴ Koma pamene cholinga changa ndi chokhumba ziri zabwino, ndipo Mulungu mu mtima mwanga akunditsogolera ine, ndipo ine ndikulephera kuwoloka phirilo, kulizungulira ilo, kudutsa pansa pa phiri, ine ndinganene kuti, “Phiri, suntha.” Mwinamwake ilo... Pamene ine ndinena zimenezo, ndipo pamene ine ndanena izo ndi mtundu uwo wa mzimu wolondola, wotsogozedwa ndi Mzimu Woyera, mu chifuniro cha Mulungu, apo pakhoza kusakhala koma supuni imodzi yokha yaing’ono yodzadza ya phiri limenelo litagumukapo, koma ilo liri pa ulendo wake. Tsiku lotsatira pakhoza kudzakhala mapaundi awiri atagwapo. Tsiku lotsatira kotala ya tani. Ndipo mwinamwake pa mwezi, madontho matani faivi. Nchiyani chimenecho? Inu mukhoza mwinamwake kusaziwona izo apobe, koma ilo likusuntha, liri panjira yake. Ine ndingakhale pomwepo ndi kumachipenyenerera chinthucho chikuchitika, chifukwa Mulungu ananena chomwecho ndipo izo zikungokhazikitsa zimenezo.

²⁵ Kodi inu mungaganizire zimenezo za amayi anu apo usikuuno? Chabwino, ngati inu mutaganizira izo, iwo akhala bwino. Chabwino. Zimenezo ndizo ngati inu mutakhulupirira izo: mungolankhula mawuwo ndipo nkukhala nawo iwo. Mukuona? Kungokhulupirira izo; kukakamira kwa izo. Ndiwo Moyo Wamuyaya.

²⁶ Tsopano, mawa madzulo... ine ndinamuza Billy, usikuuno, kuti achotsepo makadi a pemphero, ndipo ine ndimafuna kuti ndidzalankhule. Ine ndikuvomereza moona, ine ndakhala ndikuyenda kuyambira Januwale, kutsidya kwa nyanja, ndi kubwererako, mu Phoenix, kwathu komwe, ndi kubwererako, ndipo zonse kwathunthu (kuzindikira za mumtima uko) mpaka ine ndafooka kwambiri ine sindimadziwa nkomwe kuti ine ndaima kuti nthawi zambiri. Izo zimangondikwapuliratu ine.

²⁷ Ndiyeno, ine ndimayenera kuti ndizipita, ndipo iwo... inu—abale inu munandiitana ine kuti ndidzakhale kuno kwa masiku angapo. Mmene ine ndikuyamikirira zimenezo. Ine ndithudi ndikuganiza kuti ili ndi gulu lodabwitsa la azitumiki kuno. Ndikukhumba ife tikadakhala ndi nthawi pang’ono yowonjezerapo ya chiyanjano. Ngati Ambuye alola, ine ndidzabwereranso nthawiina. Osati kwa chirichonse, kumangopita tchalitchi ndi chimzake ndi kuzungulira kudutsa mzindawu ndi kudzakuhezzerani inu nonse. Ine ndidzakhala wokondwa kudzachita zimenezo: chirichonse chimene ine

ndingathe kuchita kuti ndithandizire Ufumu wa Mulungu, ndizo, ngati inu mungafune kuti ine ndichite zimenezo. Ndipo nkudzabwerera nthawi ina ndi kudzajowinana ndi ife ndi kudzakhala ndi msonkhano wabwino, wokoma kwina kwake.

²⁸ Ndipo kumbukirani, abale, ine ndidzakhala ndikukupemphererani inu. Ndicho chinthu chimodzi chotsimikizika. Ndipo ine ndikufuna inu nonse mundipempherere ine, nonse a inu.

²⁹ Ndipo tsopano ine—ndine... Mawa mmawa kudzakhala misonkhano ya tchalitchi ku matchalitchi abwino onse awa osiyanasiyana kuzungulira mzindawu.

³⁰ Tsopano, ena a magulu ochokera ku Jeffersonville ali kuno. Ena a zimzanga, mmodzi wa matrasti a mpingo, ali pano, M'bale Fred Sothmann. Ine sindinathe kukwanitsa kuti ndimuwone iye mu msonkhano. Ndipo m'bale... O, ambiri ena a zimzanga ochokera uko ku Jeffersonville, ujeni-... mlembi wanga uko ndi—ndipo onse ali kuno, penapake mu msonkhano. Ine sindinawawonebe iwo pano.

³¹ Ndipo abale, muli matchalitchi ena abwino mu mzinda uno. Ndipo alendo nonse inu, mukapezeko umodzi wa iyo ndipo mukapite ku matchalitchi amenewa mawa. Iwo akakuchitirani inu ubwino, ine ndikutsimikiza. Iwowo ndi abale amene amakhulupirira mu utumiki wa mtundu uwu. Ndi chifukwa chake iwo akhala pano pa nsanja ndi panso apo, chifukwa iwo amakhulupirira zimenezi. Ndipo ine ndimawayamikira amuna amenewo.

³² Ambuye, adalitse chaputala cha Full Gospel Businessmen ichi kuno amene—amene athandizira msonkhano uwu. Alipo... Ine ndikukhulupirira kuti ndalondola, amene athandizira msonkhano. Ine—ine ndimapita kochuluka kwa othandizira awo, chifukwa mmenemo... Ife siti yenera kukhala mwanjira iyi, koma nthawi zambiri, abale amalola kutsemphana kocheba kwambiri: monga munthu amakhulupirira *chinachake* chaching'ono, wina, *chinachake* chaching'ono; izo zimakhala ngati zimayambitsa maphokoso pang'ono ndi mabala akale kale; iwo ayenera kukhala atapola pofika nthawi ino, koma izo—izo... Ndipo ngati inu... ngati ine ndi watenga a Full Gospel Businessmen, ndiye izo zimakhala ngati zimathandizira kumangiriza izo, ndipo ife timakhala pamodzi, ndipo ife timakhala ndi chiyanjano chenicheni limodzi, basi nthawi yabwino yeniyeni. Ndipo ife timayamikira zimenezo. Mulungu adalitse chaputala chimenecho. Ine ndikukhulupirira Ambuye anachidzutsa icho ndi cholinga.

³³ Tsopano... ndiyeno ine ndinali ndi mwayi wopambana wokawona malo a M'bale Oral Roberts tsiku lina. Ndipo mai, malo aakulu chomwecho, chinthu chokongola chomwecho. Icho ndi—icho ndi chikumbutso kwa a Pentekoste.

34 Kenako ine ndinapita kwa a M'bale Tommy Osborn, malo ena odabwitsa, mwamuna wodabwitsa wa Mulungu, yemwe. . . M'bale Tommy ndi ine ndife oyandikana, ndi M'bale Oral, nayenso, basi abale apafupi kwenikweni, ndipo ife timakondana wina ndi mzake, ndipo tikuyesetsa mwakukhoza kwathu kuti tichite chirichonse chimene ife tingathe kwa ubwino wa anthu mu Ufumu wa Mulungu.

35 Chotero ine ndithudi ndikuwayamikira amuna amenewo chifukwa chokhala mu mzinda uno pakati pa amuna abwino awa amene inu muli nawo. Nkhosa inu muli ndi azibusa odabwitsa. Ine basi, ine ndinena izi monga choncho. Ambuye apitirize kukhala nanu inu nonse ndiro pemphero langa. Ndipo tsopano mawa madzulo, ine. . . Kodi msonkhano udzayamba nthawi yanji, abale? Hafu-thuu. Tiyeni tinene kuti wani—wani kapena hafu-wani inu muyenera kuti mudzakhale muli pano kuchitira kuti iwo asadzasokonezeke ndi misonkhano inayo.

36 Tsopano, ngati anyamatawo sanakuuzeni kale inu, usikuuno iwo ali ndi mabuku ena, zithunzi ndi zina zotero, ndi matepi, ndi marekodi, ndi. . . za misonkhano, ndipo iwo akugulitsa izo. Koma ife sitidzawalola iwo kuti adzagulitse izo pa Sabata, mawa. Sipadzakhala mabuku ngakhale chirichonse choti chidzagulitsidwe mawa. Chotero ife sitidzatero. . . ife sitimaloleza konse zimenezo. Ngakhale ambiri amati, “Inu mukulakwitsa moyipa. . .”

37 Ndipo Bambo wokalamba Bosworth anakonda kundiuza ine, “O, M'bale Branham, mukulakwitsa pamenepo,” koma umo ndi mmene ine ndikumverera (Mukuona?), ndipo ine—ine ndikumverera. Ngati inu mukufuna limodzi, iwo adzakupatsani inu limodzi, koma ngati inu. . . Koma ife sitingathe kugulitsa pa—pa Sabata. Ayi. Ndizo zonse. Ngati ine ndimakhulupirira zimenezo, ine ndiyenera kuzikhala moyo izo, basi. . . ine ndiyenera kuzikhala moyo ndekha. Inu mukuona? Ndipo ine—ine ndiyenera kukhala moyo mmene ine ndikumverera ndipo chotero. . . Kapena inu mukhoza kutumiza kwathu, ndi, mpaka ku nyumba, mpaka kumeneko ndi kukapeza izo.

38 Tsopano usikuuno, o, tiyeni tonse tingoiwala zimenezo, o, kuti kuli ntchito iliyonse yoti mukaigwire, kapena china chirichonse, kapena zolemetisa za mtsiku. Tiyeni tingoika kumbali chirichonse, ndipo tiyang'ane m'Mawu kwa maminiti pang'ono, ndipo tiwone zimene Mulungu angalankhule kwa ife kudzera m'Mawu Ake. Ndipo mulole ndipemphere kuti Mulungu angotipatsa ife mdalitso wawukulu kwambiri usikuuno.

39 Gene, kodi iwe unganditengere iye? Iwe unganditengere ine mtsikana wamng'ono uyo? Kodi iye si kanthu kakang'ono kokongola? Kodi iwe ungafune utapita kwathu ndi ine ndi kukasewera ndi Sarah wanga wamng'ono, wa pafupifupi kotalika chonchi? O, iwe ungafune? Ine—ine ndikufuna kuti

iwe utero. Iye ndi wa pafupifupi usinkhu wako, ndipo iye ndi mtsikana wamng'ono wa Adadi. Um-hum. Hum. Ndipo ine ndikuganiza iwe—iwe umawakonda Adadi ako nawenso, sichoncho iwe? Amayi? O, ndithudi iwe umatero. Mtsikana wamng'ono wokongola kwambiri, ine ndakhala pano, ndikumuyang'ana. Maso aang'ono owoneka ngati zibowo ziwiri zakupsya ndi moto mbulangeti ndi—ndi tsitsi laling'ono la bulauni.

⁴⁰ Ine ndimangokonda ana aang'ono okonedwa. Ine ndiri nawo atsikana awiri aang'ono kunyumba. Mmodzi wa iwo ndi Rebekah ndipo winayo ndi Sarah.

⁴¹ Kuno nthawi ina kale, ine ndinali nditachokapo. Awiri onsewo ndi atsikana aang'ono a Adadi, inu mukudziwa, ndipo ine ndimawakonda iwo. Ndipo mwamsanga iwo akangofika ine ndimayenera kuti ndiwabereke iwo, ndi. . .kungoti Becky wakula kuti azichita zimenezo; iye ndi wamkulu ngati ine. Iye angakhoze kuthyola nsana wanga tsopano; iye ndi. . .koma iye adakali mtsikana wamng'ono wa Adadi, mulimonse. Ndipo tsopano, pafupifupi chaka china, ife tikufuna tidzamtengere iye ku sukulu ya Baibulo kwinakwake ndiponso kutali ndi sukulu za wamba.

⁴² Ndiyeno, iwo anali akudikirira Adadi, inu mukudziwa, kuti afike kunyumba. Ine ndikakhala kuti ndinali ku msonkhano. Ndipo mawa usiku amakhala akundidikirira ine mpaka pakati pa usiku kuti ine ndifike. Ndipo koteru, ine ndinafika molawirira mmawa kwenikweni, pafupifupi firii kapena foro koloko. Ndipo amayi anabwera pa chitseko ndi kudzandilowetsa ine, ndipo ine ndinali wotopa kwambiri ndi wolema, ine. . .Kuno pa nsanja, ine. . .pamene. . .ukadzodzedwa umamverera bwino, koma pamene iko kukuchokera iwe, ndi pamene iwe umakhala mu vuto. Ndi angati amene anayamba azidziwapo zimenezo? Bwanji, ndithudi zimakhala choncho.

⁴³ Taonani. Eliya anapita pamwamba pa phiri ndipo anakaitanitsa moto kuchokera kumwamba, anaitanitsa mvula kuchokera kumwamba, ndipo kenako pamene Mzimu unamuchokera iye, iye amayendayenda mchipululu masiku forte ndipo Mulungu anamupeza iye, atazikokeranso ku mphanga kwinakwake.

⁴⁴ Yona, iye anapita pansu ndipo anakakhala wamoyo mmimba mwa nsomba kwa masiku atatu ndi usiku, anakalavulidwa ku gombe ndipo anakhala akulalikira. Mzinda wonsewo unalapa ndipo unabwera kwa Mulungu. Ndipo pamene kudzoda kunamuchokera iye, iye anapita pamwamba pa phiri ndipo anakamupempha Mulungu kuti awuchotse moyo wake. Mukuona?

45 Ine ndinaima pambali pa manda a William Cowper, osati kale litali, yemwe analemba nyimbo yotchuka ija imene timaigwiritsa ntchito pa msonkhano wa mgonero:

Pali Kasupe Wodzazidwa ndi Magazi,
Wotengedwa kuchokera mmitsempha ya
Emanuele,
Momwe ochimwa amadziponyera pansu pa
kusefukirako. . .

46 Kodi inu munayamba mwamvapo zimene iye. . . zinamuchitikira iye? Kudzodzako kutamuchokera kwa izo, iye anayesetsa kuti akapeze mtsinje kuti akadziphe yekha.

47 Ine ndimakhala tsidya lina la Old Kentucky Home. Ndipo Stephen Foster anamupatsa Amereka nyimbo zake zotchuka kwambiri zakumudzi. Ndipo iye akamalemba, amakhala ndi kudzodza, kudzodza kumeneko, kumalemba nyimbo, ndiye akachokamo mu zimenezo, iye amapita kukaledzera. Potsiriza, anamuitanitsa wantchito ndipo anatenga rezala ndi kudzipha.

48 Anthu samadziwa zimene anthu awo amene amakhala mu dera lauzimu amadutsamo. Tsopano *apa*, iwe umamverera ngati ukhoza kusuntha phiri. Koma ungolola kudzodzako kukuchokere iwe, ndipo nkuyambapo kutuluka pakhomo apo (ngati sipakhala munthu wina pamenepo woti akugwire iwe, mwaona) ndiyeno, mwinamwake kwa maora pang'ono, iwe umadabwa, kuti uli kuti. Ndiyeno usiku ndi usiku, zimenezo zimachotsa zabwino za iwe.

49 Ndipo pang'ono. . . Ndikufuna kuti ndikuuzeni inu za Sarah wamng'ono ndi Rebekah. Chotero mmawa wotsatira, ine ndimalephera kuti ndigone, ndipo ndinadzuka, ndinali nditakhala pa mpando, ndipo patapita kanthawi Becky, pokhala wamkulu, iye anali—anali ndi miyendo yaitali kumuposa Sarah, ndipo kotero Becky anabwera akuthamanga. . . anadzuka, analumphu pa bedi, osamudzutsa mchemwali wake wamng'ono, ndipo apa iye anabwera kudutsa mnyumbamo, akuthamanga mwaliwiro mmene iye akanathera. Iye amati, “Adadi, Adadi. . .” Ine ndinafunyulula umodzi wa miyendo yanga, ndipo iye analumphira pamenepo, nkudzakhazikika bwino bwino. Makhala ngati—mpingo wamakono, inu mukudziwa, iwo wakhala uli mu masewerowa kwa nthawi yaitali, inu mukudziwa, kwa zaka zana zingapo. Iye anakhoza kudzikhazika yekha bwino bwino, ndipo iye anaika mikono yake mondikumbatira ine ndipo anati, “O, Adadi anga, Adadi anga. . .”

50 Ndipo Sarah wamng'ono anali, ndi phokosolo, anadzuka. Chabwino, ine sindikudziwa ngati ana anu samachita zimenezo; anga amatero: Wamng'ono amatenga zosiyidwa ndi wamkulu. Ndipo chotero Sarah anali atavala zovala zogonera za Rebekah, miyendo yotalika kwambiri chomwecho, inu mukudziwa. Ndipo

apa iye anabwera, kamunthu kakang'ono kakafupi, kakugwa, kakupunthwa. Ndipo iye anafika pamenepo, mochedwerapo pang'ono. Kotero Becky anapotoloka, anati, "Sarah, mchemwali wanga, ine ndikufuna kuti ndikuuze iwe chinachake." Iye anati, "Ine ndinayamba kufika pano. Ndipo ine ndaphangira. Kotero ine ndatenga zonse za Adadi ndipo palibe chimene chatsalira cha iwe."

⁵¹ Umo ndi mmene anthu ena amayesera kuganizira za chipembedzo, sichoncho izo? Uh-huh. Uko nkulondola.

⁵² Ndipo Sarah wamng'ono wosauka, iye anagwetsa mulomo wake wawung'ono, ndipo maso ake aang'ono akuda anandiyang'ana ine, ndipo iye anayamba kulira. Ndipo Becky anali atagundanitsa chibwanu chake ndi changa, atandikumbatira ine. Ine ndimamukonda iye. Ndipo Sarah anayamba kuchokapo chifukwa Becky anali atawatenga Adadi onse. Ine ndinasuntha bondo linalo monga *chonchi* ndipo ndinalozera kwa iye monga *choncho*. O, iye anasangalala mwamsanga pomwepo ndipo anathamanga, anadzalumphira pa bondo langa chomwecho... Iye anali asanakhale nthawi yotalika kwambiri ndipo miyendo yake imalephera ngakhale kuti ifikire pansi. Iye anali ngati wovutikirapo poyenda (mwinamwake, monga ine ndimachitira, basi wovutikirapo kuyenda, inu mukudziwa), ndipo iye sanatero... amalephera kuti afikire pansi. Iye sanali chipembedzo chachikulu, inu mukudziwa, ndipo chotero iye amalephera kuti afikire pansi polimba. Iye anali asanakhale nthawi yotalika mokwanira.

⁵³ Ndipo chotero, iye amakhala ngati amavutika kuyenda, ndipo ine ndinaponyera mikono yonseyo monga *chonchi* ndipo ndinadzamukumbatira iye pafupi ndi ine, ndipo iye anadzawalitsa maso aang'ono akuda awo, ndipo anayang'ananso kwa Rebekah. Iye anati, "Rebekah, mchemwali wanga," iye—iye anati, "izo zikhoza kukhala zoono kuti iwe wawatenga Adadi wonse, koma ine ndikufuna kuti udziwe chinthu chimodzi: Adadi anditenga ine yense." Chotero...

⁵⁴ Ndizo... Chomwechonso Iye anatenga zonse za ine. Ine ndikhoza kusakhala ndi maphunziro okhoza kuikira zinthu zazikuluzo, koma basi bola ngati ine ndikudziwa Iye wanditenga ine yense, mu kulephera kuyenda kwanga, ndinamusiya kuti Iye andikumbatire ndi manja awiri onse, izo zidzangondipanga ine kumverera bwino.

⁵⁵ Chabwino, tiyeni tipereke mawu pang'ono a pemphero kwa Iye ife tisanatsegule Mawu.

⁵⁶ Tsopano, Atate Akumwamba, ife tikuzindikira kuti ife tangokhala ngati ana nafenso. Ndipo—ndipo Inu mumakonda kukhala ndi ife, ndi kudzapembedza ndi ife. Ndipo pamene ife tikukupembedzani Inu, ndipo Inu mmatikonda ife, ndipo mmatigwirizira ife mmikono Mwanu, ndipo mmatumiza Mzimu

Woyera Wanu, ndi kudzatidziwitsa ife kuti Inu muli wamoyo ndipo Ndinu Atate wathu, ife tikukuthokozani Inu mochuluka kwambiri. Tsopano, mulole Mzimu Woyera ubwere kwa ife usikuuno. Mukonde mtima uliwonse, Ambuye. Mutipatse ife mdalitso watsopano. Mutsanulire madontho a mame a chifundo pa ife, Atate. Musati muyang'ane pa machimo athu. Iwo ndi ochuluka kwambiri. Ambuye, mungowakhululukira iwo. Muwachotsepo iwo, Atate, ndipo mungotitengera ife mmikono Mwanu, ndipo—ndipo muchiritse matenda athu, ndipo—ndipo muyeretse miyoyo yathu, ndipo mumasule mizimu yathu ikhale yomasuka, Ambuye, kuti ife tikhoze kupembedza ndi kukutamandani Inu, tikhale ngati ana aang'ono tikuthamanga thamanga kuzungulira nyumba, kumadziwa kuti Adadi akuti yang'anira ife. Perekani izi, Ambuye.

⁵⁷ Tsopano, palibe munthu yemwe ali wokhoza—kuwatanthauzira Mawu. Ife tikuzindikira zimenezo. Yohane anawona Bukhu mdzanja lamanja la Iye amene anakhala pa mpando wachifumu, ndipo kunalibe munthu aliyense kumwamba, kapena padziko lapansi, kapena pansa pa dziko lapansi yemwe anali woyenera kuti atenge Bukhu kuti alitsegule ilo, kapena kumasula zisindikizo. Ndipo apo panadzabwera Mwanawankhosa, amene anali ataphedwa chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi. Ndipo Iye anali woyenera. Ndipo Iye anatenga Bukhu, ndipo anamasula zisindikizo, ndipo anadzatsegula Bukhu. O Mwanawankhosa, bwerani usikuuno. Mudzatsegule Bukhu kwa ife, Atate, pamene ife tikuyembekezera pa Inu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, Mwanawankhosa wa Mulungu. Amen.

⁵⁸ Ine ndasankha usikuuno, ndime yaying'ono ya Lemba ya mawu atatu. Koma choyamba ine ndikufuna kuti ndiwerenge ndime kapena ziwiri kuchokera mu Yohane Woyera, mutu wa 11 kuyambira ndi ndime 23.

Yesu anati kwa iye, mchimwene Wako adzawukanso.

Marita anati kwa iye, ine ndikudziwa... iye adzawukanso mu chiukitsiro pa tsiku lotsiriza.

Yesu anati kwa iye, Ine ndine chiwukitsiro ndi... moyo: iye amene akhulupirira ine, ngakhale iye atafa, komabe iye adzakhala moyo:

Ndipo aliyense amene akhala moyo ndipo nakhulupirira mwa ine sadzafa konse. Kodi mukukhulupirira izi?

Iye anati kwa iye, Eya, Ambuye: ine ndikukhulupirira kuti inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu, yemwe ayenera kubwera mu dziko.

⁵⁹ Ndipo kwa mutu ine ndikufuna kuti ndigwiritse ntchito mawu atatu awa: *Kodi Mukukhulupirira Izi?*

⁶⁰ Ine ndinawerenga nkhani nthawi ina kale. Ine ndikuganiza iyo inali nkhani yopeka. Ndipo pafupifupi atumiki nonse, ine ndikuganiza, munawerengapo bukhu la Dr. Ingraham la—la *The Prince Of The House Of David*. Ilo ndi bukhu lopambana. Ndiro, ine ndikuganiza, mwamtheradi anasiya kudinda ilo. Ine ndingakonde nditakhala nalo ilo lodindidwa, kuti ine ndidzakhoze kuliyika ilo pakati pa anthu.

⁶¹ Ndipo mmenemo, ine ndinali kuwerenga nkhani yaing'ono ya Lazaro uyu, ndi za Yesu, ndi Maria, ndi Marita, kuti, azichemwali ake a Lazaro. Ndipo ine ndinali kuwerenga mmenemo kuti kumene Yesu ankakhala, ine ndikukhulupirira, ndi Marita ndi Maria. Iwo onse awiri anali atsikana achi Hebri okoma. Ndipo Lazaro anali kuphunzira kapena amaphunzitsidwa kuti adzakhale mlembi wa ku kachisi, kumawapangira ansembe makalata a lamulo.

⁶² Ndipo Yesu amakhala ndi chiyanjano chopambana, makamaka ndi Lazaro. Pamene ife tiwerenga m'bukhu za pamene Iye amabwera ku nyumba kwawo, ndipo Marita amakhala wochedwerapo pang'ono kudzamvetsera mawu Ake, koma iye amakonza chakudya chamadzulo ndi kumakonza malo odyera, koma Maria amakhala pamapazi Ake. Ndipo Yesu ananena kuti Maria wasankha zinthu zabwino.

⁶³ Ndiyeno, ife tinawuzidwa kuti Lazaro anali iye amene anamubweretsa Yesu kwa Yohane, mu nkhani ya mabuku a Dr. Ingraham, ndi...pa *The Prince Of The House Of David*. Komabe, izo zikhoza kukhala kuti sizinali zoono, ine sindikudziwa, koma basi kuti tiike maziko a nkhaniyo, koma Iye ayenera kuti ankakhala ndi iwowo.

⁶⁴ Tsopano, ife takhala tikuphunzira sabata ikubwerayi, yatha iyi, kani, kuti Yesu ananena mu Yohane Woyera 5:19, “Ine... Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha, koma chimene Iye awawona Atate akuchita: momwemonso Mwana amachitira. Atate amagwira ntchito ndipo Mwana amateronso.” Mukuona? “Zimene Iye awawona Atate akuchita.”

⁶⁵ Chotero kuti aipange iyi kukhala nkhani yeniyeni yolondola, Atate, Mulungu, ayenera kuti analankhula ndi Mwana Wake, Yesu, ndipo anati, “Mzako, Lazaro, afa, koma izo zichitika kwa ubwino, kotero Iwe uchoke pakhomopo. Upite kutali, chifukwa adzakufunsa kuti Iwe umupempherere iye, kapena, umuchize iye, ndipo—ndipo Ine sindikufuna kuti Iwe uchite zimenezo.” Ngati inu mungaiyang'anitsitse nkhaniyo pamene ife tikupitirira, inu mudzawona kuti iyo ikuthera kwa choonadi chomwecho cha izo. Chotero, Yesu, basi wopanda kutsanzika kulikonse kapena chirichonse, anachokako kunyumbako ndipo anapita kwinakwake, sanabwerere usiku umenewo. Ndipo Iye anapita ku mizinda ina. Ndipo mwamsanga pamene Yesu anachoka pakhomopo, pamenepo mavuto anayambika.

⁶⁶ Ndipo pamene Yesu achokapo pakhomo panu, mavuto amakhala ali panjira. Ingokumbukirani, pamene Iye achoka pakhomo panu, mavuto amayambikapo. Pamene inu mukhala ndi zosangalatsa ndi chirichonse zikugwira ntchito mu tchalitchi chanu mwangwiro kwambiri, monga chi Rickenbacker cha masilinda sikisitini chachikulu, ndipo inu nkumusiya Yesu mu zimenezo, pamene Yesu achoka pa tchalitchi chanu, mavuto amakhala ali panjira. Inde, bwana, pamene Yesu achisiya chipembedzo, kuti iwo amuka Iye pambali ndikuti, “Chabwino, tsopano ife sitikukhulupirira basi kuti zinthu izi zikhoza kukhala ndendende basi,” ndipo inu nkuchivomereza chinthu chinachake, mavuto amakhala ali panjira. Muzingokumbukira zimenezo.

⁶⁷ Zikundikumbutsa ine za nkhani ya Ambuye Yesu, imene imapezeka mu Bukhu la Luka. Inu mukudziwa pamene Iye anali mnyamata chabe wa pafupifupi usinkhu wa zaka thwelofo, anthu Ake anamutenga Iye, monga unali mwambo wake chaka ndi chaka, kuti amapita ku phwando la Pentekoste. Ndipo pamene iwo anali mu mzinda wa Yerusalemu ku phwando ndipo akukhala ndi nthawi yabwino, ife tikupeza mu Baibulo, kuti iwo anayenda masiku atatu wopanda Iye. Ndipo iwo ankaganiza kuti mwinamwake, anangozitenga izo mwachizolowezi, kuti Yesu ayenera kuti ali pakati pa ena a achibale awo. Tsopano, ife sitingathe kuchita zimenezo. Pamene iwo anabwera kuti amfufuze pakati pa achibale awo, Iye kunalibeko kumeneko.

⁶⁸ Ndipo ife sitingazitenge izo mwachizolowezi, basi chifukwa chakuti ndife Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Apentekoste, ndipo maziko athu ndi makolo athu anali okhulupirira amphamvu, ife nkungozitengera izo, chabwino, mwachizolowezi, Yesu ali nafe ife. Ife sitingathe kuchita zimenezo. Ife tiyenera kukhala mchilumikizano ndi Iye tsiku ndi tsiku ndi miniti iliyonse. O, ine ndimazikonda zimenezo.

⁶⁹ Ine ndikufuna chimene Mulungu ali tsopano. Chimene makolo anga anali nacho, chimene makolo a mmbuyo anali nacho, chinali chodabwitsa, koma (Chimene iwo anali nacho ndi chabwino.) Ine ndikuganiza ife tapita patali mu ulendowu.

⁷⁰ Tiyeni tiwone chimene Iye ali lero. Ine sindikufuna kuti ndiziyang’ana mmbuyo ndi kukawona chimene Bambo Moody anachita, chifukwa ife tiri patali mu ulendowu kuposa Bambo Moody. Limene liri vuto ndi mipingo yathu: ife timayang’ana mmbuyo ndikuti, “Chabwino, tiyeni tiwone zimene Bambo John Wesley ananena, zimene ena a enawo ananena.” Ndi chifukwa chake sayansi yapita patali kwambiri mu zochita zake, kuposa mmene chipembedzo chiliri mu zake.

⁷¹ Kuno zaka firii handiredi zapitazo, wa sayansi wa chi French anatsimikizira kuti ngati iwe ungathamange liwiro lowopsya la mamailosi sate-faivi pa ora, mphamvu yokokera pansa

ingakuchotse iwe padziko lapansi. Inu mukuganiza kuti sayansi ingalozere mmbuyo kwa zimenezo lero? Iwo akumathamanga mamailosi naintini handiredi pa ora ndipo nkumapitirirabe. Iwo akuthamangira patsogolo, akuyang'ana mtsogolo. Koma ife timafuna kuti tiziyang'ana mmbuyo ndi kukawona zimene Moody ananena; Sankey ananena; Finney ananena; Knox, Calvin; ena a iwo. Zimene iwo ankanena zinali zabwino. Zimenezo zinali za m'badwo wawo, koma ife tikupitirira chitsogolo.

⁷² Agogo anga aamuna anakwera ngolo. Ine ndikuyendetsa Ford V8. Mwana wanga adzawulutsa ndege. Ndizo, ife tikuyenda chitsogolo. Ndi chimene chipembedzo chiyenera kukhala. Kudza kwa Ambuye kwayandikira. Mpingo uyenera kuti udzisunthira chitsogolo kukalowa mu mphamvu zake. Sayansi ikhoza kungokwera mpaka apa ndipo kenako iyo iyenera kugwera pansu, koma ife tiri ndi magwero osayamba, amene sanayambe akhudzidwapo, a mphamvu, yopanda malire, ya Mulungu, imene ife tiyenera kuti tidzisunthiramo. Ife tikukhala moyo wodzimana mwayi wathu mamailosi milioni usikuuno, mwayi umene Akhristu ayenera kuti azisangalala nawo. Ine ndimadzichitira ndekha manyazi pamene ine ndiyang'ana uko ndi kuwona kokhalako anthu, ndi matenda, ndi mavuto amene akuchitika pakali pano. Mpingo wathu umayenera kuti uziyenda mu msewu, kumachiza odwala, kumaukitsa akufa, kumatulutsa ziwanda, kumachita zizindikiro ndi zodabwitsa, kumalipangitsa dziko lonse kuzindikira kuti Yesu Khristu ali moyo. Ndicho chimene ife tikusowa kuti tizichita.

⁷³ Bwanji, inu mukuti, “Bambo Moody sanati...” Bambo Moody samakhala moyo mu tsiku lino. Uko nkulondola. Ife tikukhala mu Kudza kwa Ambuye. Ndipo ife tangozitengera izo mwachizolowezi kuti Iye amakhala ndi achibale athu. Koma tsiku lina pamene wandewu anamutsutsa Bambo Graham, ife tinadzapeza kuti Iye sanali pakati pa achibale athu.

⁷⁴ Kodi iwo anakamupeza kuti Iye? Ndikuti—ndikuti kumene anakamupeza Yesu? Komweko kumene iwo anamusiya Iye. Kodi iwo anamusiya kuti Iye? Pa phwando la Pentekosite. Kodi ife tamusiya kuti Yesu, nkuti kumene mpingo? Pa phwando la Pentekosite. Pamene ife tichokako ku mphamvu ya nthawi yakale iyo ya Pentekosite ndi phwando la Pentekosite, ife timakhala kuti tikuchoka kwa Yesu. Ndiko kulondola ndendende, mzanga. Ife tikudzimana tokha mwayi wathu. Inde, bwana.

⁷⁵ Iwo anamusiya Iye pa phwando la Pentekoste, ndipo amenewo ndi malo okhawo amene Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, ndi Apentekoste adzamupeze konse Iye, ndi kubwerera kumene inu munamusiya Iye. Chiri kuti chimwemwe cha Ambuye? Ili kuti mphamvu ya Ambuye? Mpingo ukufunsa lero, “Chiyani—chinachitika chiyani ndi Mulungu wa

mbiriyakale?” Iye akudikirira anthu Ake kuti amuitanitse Iye powonekera. Koma a . . .

⁷⁶ Ife sitingathe kuchita izo podzera mu zipembedzo. Ife sitingathe kuchita izo pansi pa kuwerenga maganizo. Ife sitingathe kuchita izo pansi pa masamu, kapena ife sitingathe kuchita izo ndi maphunziro. Ife tadzilekanitsa tokha, tadziganizana tokha. Ife si ogawanika. Ife tiri munthu mmodzi ndithudi mwa Khristu Yesu. Ife ndife tonse mmodzi mwa Khristu, ndipo zipembedzo zathu sizidzachita konse zimenezo. Zabwino monga izo ziliri, izo zizingachite izo. Maphunziro athu ndi cholepheretsa chachikulu chimene Uthenga unayamba wakhalapo nacho, ndicho maphunziro.

⁷⁷ Chimene ife tikusowa si maphunziro. Ife tikusowa mphamvu ndi chiwonetsero cha Mzimu Woyera zitabwerera mu mpingo kuti ziwonetsere mphamvu. Yesu sananene kuti, “Pitani ku dziko lonse ndipo—ndipo mukaphunzitse.” Iye sanene kuti, “Pitani ku dziko lonse ndipo mukachite. . .” Iye anati, “Pitani ku dziko lonse ndipo mukalalikire Uthenga.” Ndipo Uthenga ndi kuwonetsera mphamvu ya Mzimu Woyera, chiwukitsiro. Ife tikadali operewerabe pano mamailosi millions kuposa kumene ife tiyenera kukakhalako. Tiyezi tisonthire chitsogolo. Tiyezi tibwerere mmbuyo kumene ife tinamusiyira Iye pa phwando la Pentekosite.

⁷⁸ Yesu ananena, mu Yohane, ine ndikukhulupirira, mutu wa 15, Iye anati, “Ine ndine Mpesa; inu ndinu nthambi.” Chabwino tsopano, ngati Mpesa umenewo unaika nthambi yoyamba, ndipo kuchokera mwa nthambi imeneyo analemba Bukhu la Machitidwe, nthambi yachiwiri idzapanga Bukhu lina la Machitidwe. Nthambi yachitatu idzapanga Bukhu lina la Machitidwe. Ndipo nthambi iliyonse imene iti idzabwere mwa Mpesa umenewo idzakhala chimodzimidzi monga nthambi yoyamba inali.

⁷⁹ Tsopano, inu mukhoza kumezanitsa, ife tikudziwa zimenezo. Ine ndawonapo mtengo wa zipatso uli ndi zipatso za mitundu eyiti zosiyanasiyana. Ine ndawonapo mtengo wa lalanje ukubereka manyumwa, ndi mandimu, ndi china chirichonse pa iwo, koma izo zinachita kumezanitsidwamo.

⁸⁰ Ndiro limene liri vuto lero. Ife tamezanitsamo malingaliro athu, tamezanitsamo zipembedzo zathu, koma ngati mtengo umenewo uti udzaike konse mpesa wa chipatso, pawokha, iwo udzakhala wofanana ndi wapachiyambi uja umene unalowa mmenemo. Alaluya! O, mpingo udzalumikizana pamodzi, koma ife tikusowa mphamvu ya wapachiyambi. Ife tikusowa Mzimu Woyera, mphamvu ya chiwukitsiro cha Yesu Khristu. Ndicho chimene Iye anatuzaza ife kuti tizichita.

⁸¹ “Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi.” Ngati mtengo wa mpesa udzaika mphukira ina, ndipo iyo nkubwera ndi

mphesa za buluu zokongola, mpesa wotsatira umene udzatulutse udzakhala ndi mphesa za buluu zokongola. Ngati Mpesa woyamba utatulukira, ndipo iwo anagwa ndi kukhudza kwa Mzimu Woyera, ndipo anachita zozizwitsa zazikulu, ndi zizindikiro, ndipo anasindikiza umboni wawo kwa dziko... Ngakhale ambiri a iwo ndi umboni wawo, iwo, ndi magazi awo, iwo anasindikiza umboni wawo. Iwo anadutsa mitundu yonse ya zowawa ndi chirichonse kuti adzabweretse Uthenga. Iwo anavutika; iwo anamenyedwa; iwo analangidwa. “Kodi ife tinyamulidwe popita kwathu Kumwamba pa kama wa maluwa wophweka, pamene ena anamenyera kuti apate mphotho, ndipo anayenda kudutsa nyanja za magazi?” Kodi ife tikuyembekeza kuti tichita chiyani? “Ne ndiyenera kumenya ngati ine ndiyenera kulumulira. Wonjezerani kulimbika kwanga, Ambuye.” Ndithudi. Ife tikusowa. . .

⁸² Ife sitikusowa chipembedzo chatsopano. Ife sitikusowa nyumba ya tchalitchi yatsopano. Chimene ife tikusowa lero ndi chitsitsimitso chachikale cha kuchire, cha mmwamba mwa buluu, chakupha tchimo cha Chipentekosite, chimene chinabadwira pa Pentekosite ndipo chabwereranso mu tchalitchi kachiwiri, mphamvu ya Mzimu Woyera kachiwiri, kuti chidzamubweretse Yesu powonekera.

⁸³ Mulungu wa mbiriyakale nthawizonse amabwera powonekera mu nthawi yovuta. Ife timazisowa zimenezo. Ndiro limene liri vuto ndi mpingo wathu lero. Ife tikubwerera mmbuyo kwambiri. Ife tikugwera mu mafashoni a mdziko. Ndipo pang’ono ndi pang’ono, chaka ndi chaka, izo zikuyamba kumafa pang’ono ndi kumafota.

⁸⁴ Kukhala nthawi yotengulira posachedwapa. Mulungu adzaidulanso iyo motsimikiza basi monga ine ndaimirira pa guwa lino. Mulungu adzamudulanso iye ndicholinga chakuti adzamupange iye kuti azibereka chipatso. Iye adzadula ntchito za chidziko kudzichotsa mmenemo limodzi la masiku awa. Chamanyazi choterocho, momwe mpingo wapitirira pansu pa dzina la chipembedzo.

⁸⁵ Ndipo ife tikupeza kuti, pamene Yesu anachoka, imfa inabwerapo. Pamene Yesu achoka pa mpingo wathu, mphamvu ya Mzimu Woyera imachoka pa mpingo wathu, iwo umayamba kufota ndipo—ndipo umafa. Ndipo pakapita kanthawi sipamakhalanso kalikonse kwa iwo. Tsopano, pamene Yesu anadzachoka, imfa inabwerapo. O, ndi nthawi yachisoni bwanji imene iyo inali.

⁸⁶ Ndipo zindikirani, iwo anali akusinkhasinkha, ndipo iwo anamutumira Yesu, koma Iye sanabwere. Iwo anamutumiranso Iye kachiwiri, ndipo Iye sanabwere, koma Iye ankadziwa chimene Iye akanati adzachte. Iye akudziwa usikuuno, chimene Iye ati achite. Palibe chimene chataika ndi Iye: Iye akudziwa

ndendende chimene Iye akukonzekera kuti achichite. Iye awadzutsa anthu, motsimikiza basi monga ine ndikuimira pa guwa ili. Iye adzawadzutsa anthu kwa Dzina Lake kuchokera mu kam'badwo ka Amitundu. Iye achita zimenezo.

⁸⁷ Ndi nthawi ya Ayuda imene ili pafupi tsopano, ndipo ya Amitundu ikutha, chifukwa iwo angotuluka kumene. Iwo akumukana Khristu; iwo akukana zizindikiro zawo; iwo akukana chirichonse chimene chimatchedwa umulungu, ndipo akumachitchula icho ngati mtundu wina wa zowerenga maganizo kapena mphamvu ya mdierekezi ndi kumachita... Iwo akuchitira mwano Mzimu Woyera ndipo akudzisindikizira okha kutali ndi Mulungu. Ndipo Mulungu adzatenga apang'ono amenewo, pakapita kanthawi, ndipo adzawakweza iwo kudzakhala Mpingo wamphamvu, ndipo kenako adzatembenuzira Mzimu kwa Ayuda, ndi kudzawutengera Mpingo wa Amitundu kwawo. Kulondola ndendende. Iye akupangidwa tsopano. O, motani, ife tiri pamapeto a nthawi, pafupifupi.

⁸⁸ Yesu, Iye ankadziwa. Ndipo patapita kanthawi Iye anati, “Bwenzi wathu, Lazaro, akugona.”

⁸⁹ Bwanji, ophunzira amaganiza kuti iye anali kupuma pang'ono. Iye anati, “Chabwino, ngati iye akugona, iye akuchita bwino kwambiri.”

⁹⁰ Chabwino, Iye ananena mu Ake... nkalankhulidwe kawo, kuchitira kuti iwo amvetse, anati, “Iye wafa, ndipo chifukwa cha inu Ndine wokondwa kuti Ine kunalibeko kumeneko.” Mukuona? “Chifukwa cha inu, Ndine wokondwa kuti Ine kunalibeko kumeneko.” Chifukwa iwo bwenzi akumufunsa Iye kuti—kuti amuchiritse—kuti amuchiritse iye, koma Iye amadziwa kuti Iye sakanatha kuchita zimenezo, chifukwa masomphenya anali alipobe... atadutsa masiku anayi amenewo Iye anadziwa kuti imeneyo inali nthawi imene Atate anamuza Iye. Nzokongola bwanji; Iye ananena ku manda, “Atate, Ine ndikukuthokozani Inu, Inu mwandimva kale, koma Ine ndikungonena izi chifukwa cha awa amene aimirira.” Mukuona? Iye anali akudziwa kale zimene Iye akanati adzachite. Iye anati, “Ine ndipita ndikamudzutse iye.”

⁹¹ Tsopano, ine ndikukhoza kulingalira khomo laling'ono ilo linali litasweka kwenikweni. Yemwe amagula buledi anali atapita, chisoni. O, zimakhala zodabwitsa pamene iwe ukhala ndi khomo lachisoni kapena mtima wachisoni, ndipo kenako Yesu nkudzawonekera mwakamodzi, sichoncho izo? Ine ndikukhoza kulingalira ndikumuwona Marita, mkazi wamng'ono wokongola atadziphimba ndi chophimba chakuda pa nkhope yake, ndi Maria wamng'ono, ndipo iwo atagwirana wina ndi mzake, akuti, “Kodi ife tichita chiyani? Ababa ndi Amama anapita, ndipo mchimwene wathu wofunikira...

Tsopano, ife tinasiya tchalitchi, ndipo ife tinachotsedwa kwa iwo, ndipo tinabwera kuti tidzamutsatire Yesu waku Nazareti. Ndipo Iye anachokapo ndipo anatsiya ife, kwinakwake.”

⁹² Ine ndikukhoza kumumva wotsutsa atabwera pafupi ndikuti, “Hei, ali kuti Wochiritsa Wauzimu uja, Mneneri uja waku Galileya? Ali kuti Iye tsopano? Mwaona, pamene inafika nthawi yeniyeni yoti Iye achite chinachake, Iye anali atapita.” Ndi zimenezotu. Mwaona, Mulungu amangokonda kuchita zimenezo, basi ndi cholinga chakuti anthuwo, basi, kungofuna kuti anthuwo awonetsere chimene iwo ali, eya, amangwayesa iwo kuti awone chimene iwo ali kwenikweni. Iye amawapatsa iwo mdalitso. Iye amawonekera, amadzisonyeza Yekha, amadziwonetsera Yekha kwa anthu, ndicholinga chakuti awone kuti iwo achita motani, kungofuna kuti awone chimene iwo angachite pa izo.

⁹³ Tsopano, ife tikupeza ndiye, patapita—masiku pang’ono, masiku anai, Lazaro wosauka anafa. Iwo anakamuika iye. Tsiku lachiwiri, tsiku lachitatu, tsiku lachinai. . . Tsopano, aliyense akudziwa chivundi chimayambika pakadutsa masiku atatu: mphuno imagwera mkati pa nkhope, poyamba. Ndipo zikatero chivundi chimayambika; mphutsi za pakhungu zimayamba kudya thupi. Iwo anakamuika iye mnthaka, anaika mwala wawukulu pamwamba pa mphanga imene iwo anamuikako iye. Ndipo apo ndi apo, atsikanawo amatha kupitako ndi kukagwadwa pansu pa mandapo ndi kumalira.

⁹⁴ Ndipo patapita kanthawi, zinamveka konsekonse, “Yesu wabwera. Ife tamuwona Iye akuyendayenda mu mzinda.” O, Marita wamng’ono uja, yemwe anakhala, mowonekera kwambiri, wochita mochedwerapo za izo, iye anatsimikizira pamenepo kuti iye anapangidwa ndi chiyani. Apa iye anabwera. Akubwera panjira yake ndiye, akuthamanga pofunafuna. Ine ndikukhoza kuwamva ena a iwo mumsewu akuti, “Chabwino, ine ndikuganiza iwe wakhutitsidwa tsopano, kuti chipembedzo chanu chinali chabodza.” Iye sanawasamale iwo ndipo anapitirira, anadutsa ndithu otsutsa onse. Iye anatsikira kumusi mpaka iye anamuwona Iye, mwinamwake atakhala pansu pa ngodya ya msewu.

⁹⁵ Tsopano, mwakuwoneka, iye ayenera. . . iye akanakhoza kukhala nawo ufulu womuzazira Iye ndi—ndi kumulankhulira Iye zoipa. Bwanji, iye sanathamangireko ndi kukati, “Tayang’anani kuno, tayang’anani kuno, Inu. Inu mumayenera kukhala Mneneri, Munthu wa Mulungu. Bwanji Inu simunabwere pamene ife timakuitanani Inu? Bwanji, ndife chinthu chosedwa cha mtawuniyi tsopano. Ife tinachoka mtchalitchi chathu kuti tidzakutsatireni Inu.” Zimawoneka ngati iye anali nawo ufulu. Koma inu mukudziwa, chimodzimidzi monga ine ndinalalikira za, *Mwanawankhosa Ndi Nkhunda*, ngati ndife mwanawankhosa, mwanawankhosa

amapereka ufulu uliwonse umene iye ali nawo. Ndiko kulondola ndendende. Iye samakhalanso ndi kalikonse koma ubweya, kotero iye amayenera kuwupereka umenewo. Ndipo iwe umapereka ufulu uliwonse umene iwe uli nawo ndi cholinga chakuti umutumikire Mulungu. Ndiko kulondola ndendende.

⁹⁶ Ine ndimawazazira akazi za mmene iwo akuvalira tizovala takale tating'ono iti, inu mukudziwa, ndipo iwo anati, "Chabwino, ndife—ndife Achimereka. Ife tikhoza kuchita zimene ife tikufuna kuchita."

⁹⁷ Ine ndinati, "Ndiko kulondola ndendende, koma ngati ndiwe mwanawankhosa, iwe ungapereke mafulu ako." Kusuta ndudu ndi kumapitirira monga choncho, ndicho chinthu choipitsitsa mkazi anayamba wachichitapo. Ndiko kulondola ndendende.

⁹⁸ Dona ananena ndi ine, osati kale litali, akulankhula ndi ine, anati, "Koma, M'bale Branham, iwo sakupanga mtundu wina uliwonse wa zovala."

⁹⁹ Ine ndinati, "Koma iwo akupangabe makina osokera ndipo akugulitsabe nsalu. Palibepo chowiringula za izo nkomwe." Ndiko kulondola ndendende.

¹⁰⁰ Kumbukirani, tsikulina, inu mukhoza kukhala wangwiro kuno kwa amuna anu, koma inu mudzakayankhira chigololo chifukwa cha izo, motsimikiza basi: "Aliyense amene ayang'ana pa mkazi namukhumbira iye, wachita naye kale chigololo mu mtima mwake."

¹⁰¹ Vuto ndi chiyani ndi akazi Achipentekosite lero, ndi chimene ine ndikudabwa. Mmene inu mwachokera ku mzere wa mpanda wa kale. Mmene amayi anu anakonda kukhalira ndi tsitsi lalitali, ndipo lero akazi Achipentekosite akumazipenta ngati gulu la Mardi Gras, ndipo akumadula tsitsi lawo, ndi kumavala zovala zakale zazing'ono zazifupi monga choncho, chimodzimodzi basi monga onse a mnjirayi... kumatuluka panja ndi kumakatchetcha pabwalo madzulo, pamene amuna akudutsa, kodi inu mukuzindikira, mkazi, kuti inu mudzayenera kuti mudzakayankhe chifukwa chochita chigololo ndi amuna amenewo? Inu mukudzipereka nokha kwa iwo ndi cholinga chimenecho. Ndi mzimu woipa pa mpingo ndi anthu, ndipo iwo sakudziwa izo ayi. Akhungu ndipo sakudziwa izo. Icho ndi choonadi.

¹⁰² Mwinamwake inu mukhoza kunena kuti ine ndiribe ufulu wonena zimenezo ngati mlaliki. Chabwino, ine—ine ndiyenera kutsatira kutsogolera kwa Mzimu Woyera; ndizo zonse zimene ine ndingathe kunena. Inu. . . Ngati ine ndidzakumane nanu inu pa chiweruzo, ndiye ine sindidasowa kudzakhala ndi magazi anu mmanja mwanga. Muchokeko kwa chidutswa chirichonse cha mnthaka chimene chimawoneka ngati Satana. Mutalikirane ndi zimenezo. Muchokeko kwa izo. Ine sindikusamala kaya ndi

akatswiri angati apa kanema. . . Inu simuli kuno, kudzakhala katswiri wapa kanema; ndinu mwana wamkazi wa Mulungu.

¹⁰³ Ndinalalikira mu tchalitchi cha m’busa mmawa wina, za kapolo wakale, panthawi imene iwo ankagulitsa akapolo kale kale. Ndipo iwo anakonda kubwera ndi kumadzawagula iwo pa okushoni. Ndipo anthuwo anali, iwo ankalira, kumafuula, chifukwa cha dziko la kwawo; iwo sadzabwererakonso nkomwe. Ndipo iwo ankachita kumawakwapula iwo. Ndipo iwo ankawagula iwo chimodzimidzi basi monga momwe inu mungagulare galimoto, basi kwa chirichonse, mitengo, ndipo nkumawagulitsa anthu amenewo.

¹⁰⁴ Ndipo tsiku lina, wogula anabwera, wogulira ena, anabwera ku maziko aakulu- . . . munda wawukulu, kani. Ndipo iye anati, “Ndi akapolo angati amene muli nawo kuti mugulitse?”

¹⁰⁵ Anati, “Chabwino, ine ndiri ndi ena osinthanitsa.” Iwo amayesetsa kuti atenge okulirapo. Atenge amayi amenewo, abambo. . . Ngati mkazi amene anamukwatirayo anali mkazi wamng’ono wofooka, amatenga azibambo aakulu athanzi awa ndi kukawakweranitsa iwo ndi. . . ngati akavalo ndi zinyama. Sizinali zabwino nkomwe. Mulungu anamupanga munthu. Munthu anapanga akapolo. Izo sizoyenera kuyamba ndi kuyamba, ayi. Mulungu sanakonze kuti munthu aliyense adzakhale kapolo. Ayi, bwana. Ndipo ayi. . . Penyani zimene zinkachitika.

¹⁰⁶ Ndiye mkati mwa zonsezo, munthu uyu anati, “Chabwino, ine ndikufuna ndigule ena a iwo. . .” Iye anamuzindikira mnyamata mmodzi pamenepo. Iwo samasowa kuchita kumukwapula iye. Chibwanu chake chimakhala mmwamba, mutu mmwamba, basi ngati njonda yeniyeni, akuyendayenda. Ndipo wogula uja anati, “Ine ndikufuna kuti ndimugule iye.”

¹⁰⁷ Iye anati, “Koma iyeyo si wamalonda.”

¹⁰⁸ Iye anati, “Chabwino, chifukwa chiyani?” Anati, “Kodi iyeyo ndiye bwana?”

¹⁰⁹ Iye anati, “Ayi, iye ndi kapolo.”

¹¹⁰ “Chabwino,” anati, “chifukwa chiyani? Kodi inu mumamudyetsa iye bwinoko kusiyana ndi onse a iwo?”

¹¹¹ Iye anati, “Ayi. Iye amakadyera kophikira uko limodzi ndi ena onse a iwo. Iye ndi kapolo.”

¹¹² Anati, “Nchiyani chikumupangitsa iye kukhala wosiyana kwambiri kuposa ena onse a iwo?”

¹¹³ Ndipo bwanayo anati, “ine ndinkadabwa zimenezo inemwini kwa nthawi yaitali, koma tsiku lina ine ndinadzapeza. Uko ku dziko la kwawo, bambo ake ndi mfumu ya fuko. Ndipo ngakhale iye ali wobwera ali kutali ndi kwawo, iye amadziwabe kuti iye ndi mwana wa mfumu ndipo iye amakhala khalidwe lakuti ndi iyeyo.” Ngati zimenezo. . . Ngati mbadwa yaku Afrika

ingakhoze kuzindikira kuti bambo ake ndi mfumu, ndipo ali kuno mlendo mu dziko la chilendo nkukhoza kumadziwabe kuti kuwoloka nyanja iyeyo ndi mwana wa mfumu, ayenera chotani amuna ndi akazi kumakhala akhalidwe iwoeni pamene inu muli ana aamuna ndi aakazi a Mulungu? Kumachita monga chomwecho. Ndithudi. Kumakhala akhalidwe; kudziyeretsa nokha ndi kumachita monga ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Nzosadabwitsa, chikhalidwe chotani.

¹¹⁴ Ndi ife pano. O, Marita wamng'ono, anabwera akuthamanga. Iye ankawoneka ngati anali nayo—njira yolankhulira chinachake momutsutsa Iye. “Chifukwa chiyani Inu simunabwere kwa mchimwene wanga? Taonani zimene ife takuchitirani Inu, ndipo Inu mwatikhumudwitsa ife.” Chabwino, ngati iye akananena zimenezo, nkhaniyo sibwenzi itathera momwe iyo inachitira. Ayi, bwana. Ndi mmene inu mumafikira pa mphatso Yauzimu ya Mulungu. Ngati Mulungu atumiza mphatso, inu mumayenera kuti mudziifikira iyo moyenera. Ngati inu mukuyembekeza kuti mupeze chirichonse kuchokera kwa iyo, inu mumayenera kuifikira iyo moyenera. Ndipo Marita ankadziwa zimenezo. Iye mwina awake anali atawerenga za mkazi wa Chishunemu ndi mwana wake. Ndipo iye . . . Ngati mkazi wa Chishunemu uja anadziwa kuti Mulungu anali mwa Eliya, ndi mochulukwa bwanji Iye anali mwa Yesu? Zedidi.

¹¹⁵ Chotero, iye anapitako ndi mafikidwe oyenera. Iye anathamangirako ndipo anakagwa pansu pa mapazi Ake. Ine ndimazikonda zimenezo! Anagwa pansu pa mapazi Ake ndipo anati, “Ambuye. . .” Ndiwo udindo Wake woyenera. Ndicho chimene Iye anali. Iye anali Ambuye wake. “Ambuye, ngati Inu mukadakhala kuno, mchimwene wanga sibwenzi atafa.”

¹¹⁶ O, mai! O, ine ndikukhoza kulingalira ndikuwuwona mtima Wake wawukulu pamene Iye ankayang'ana pa mkazi wokongola uyo, misonzi ikutsikira mmunsi mwa masaya ake. Anati, “Ambuye, ngati Inu mukadakhala kuno, mchimwene wanga sibwenzi atafa.” Penyani zimene iye ananena. “Koma ngakhale tsopano, Ambuye, ngakhale iye wafa, ngakhale mphutsi za pa khungu zikuyenderera pa thupi lake, ngakhale tsopano, Ambuye, chirichonse chimene Inu mungampempe Mulungu, Mulungu akupatsani Inu chimenecho.”

¹¹⁷ O, ndicho chinsinsi chake. Inu mukhoza kunena kuti, “ine ndapita ku chipatala chirichonse. Adokotala akunena kuti ine ndifa, koma ngakhale tsopano, Ambuye. . . Ndine wolumala ndi nyamakazi; ine ndikulephera kuyenda, koma ngakhale tsopano, Ambuye. . .”

¹¹⁸ Mwana wamng'ono uyo anali ndi mutu wa madzi wawukulu *choncho* usiku wathawu. Palibe chirichonse chimene inu mukanatha kuchita. Iwo akanayenderera ndipo

akanaphulitsa mutu wake wawung'ono ndipo akanafa, “Koma ngakhale tsopano, Ambuye. . .” Iye akadali Mulungu yemweyo. Iye akadali Ambuye yemweyo. “Ngakhale tsopano, Ambuye. . .” Ndipo Iye akukhala pa dzanja lamanja la Mulungu Wamphamvuzonse, akukhalira pakati zinthu zimene ife timadzinenera kuti Iye watichitira.

119 Tsopano, ine ndikumverera mwachipembedzo kwenikweni. Ndithudi ndikutero. Inu munditcha ine woyera wodzigudubuza, kotero inu mukhoza kungoyambiratu, ndipo muthane nazo izo.

120 Chotero, inde, bwana, “Ngakhale tsopano, Ambuye, chirichonse chimene Inu mungampemphe Mulungu, Mulungu achichita icho.”

121 “Apempheni Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho,” Yesu anatero.

122 “Ngakhale tsopano, Ambuye, chirichonse chimene Inu mungapemphe, Mulungu adzakupatsani Inu icho.” O, zimenezo ziyenera kuti zinasuntha mtima Wake wawukulu.

123 Iye anati, “Mchimwene wako akhalanso moyo.”

124 Iye anati, “Eya, Ambuye. Iye adzakhalanso moyo. Iye anali mnyamata wabwino. Iye adzawukanso mu chiwukitsiro cha onse pa tsiku lotsiriza.” Ayuda amenewo amakhulupirira mu chiwukitsiro cha onse. “Iye adzatulukira mu chiwukitsiro cha mmasiku otsiriza.”

125 Tayang'anani pa Iye. Iye anadzikokera Yekha pamodzi. Iye anati, “Ine ndine Chiwukitsiro ndi Moyo.” O, mai. Panalibepo munthu nkale lomwe amene akananena zimenezo. Sipadzakhalaponso wina mtsogolo, adzathe kunena zimenezo. Iye ali Mmodzi yekhayo amene anganene zimenezo. “Ine ndine Chiwukitsiro ndi Moyo,” atero Ambuye. “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye anali wakufa, komabe iye adzakhala wamoyo. Ndipo aliyense amene akhala moyo ndipo nakhulupirira mwa Ine sadzafa konse. Kodi mukukhulupirira izi?”

126 Iye anati, “Eya, Ambuye.” O, iye anadziwa kuti chinachake chinali kukonzekera kuti chichitike. Chiyenera kutero.

127 Pamene chikhulupiro chochokera mu mtima woona chikomana ndi Mulungu, zimano zimenezo zimangolumana pamodzi monga *choncho*. Chinachake chiyenera kuchitika. Ine ndikukubetcherani omvetsera inu usikuuno, mu Dzina la Yesu Khristu, mukalola chikhulupiro chanu chilumikizane ndi Mulungu monga *choncho*, mu maminiti pang'ono ife tidzakhala ndi Pentekosite ina. Padzakhala chitsitsimutso choterocho chiti chidzasefukire mu mzinda uno, sipangakhale apolisi okwanira mu dzikoli oti awatontholetse iwo. Uko nkulondola. Pangakhale chitsitsimutso chenicheni. “Ngakhale tsopano, Ambuye. . .”

128 “Chabwino, Ambuye, ife tagwidwa mu *izi*; ife tachita *izi* ndipo tachita *izo*.” Ine sindikusamala zimene inu mwachita, “Ngakhale tsopano, Ambuye...” Iye akudikirira kuti inu muitanire pa Iye. Iye... “Kodi mukukhulupirira izi?” Zedi. Inde, bwana. “Ngakhale tsopano, chirichonse chimene Inu mudzamufunsa Iye...”

129 “Kodi mwakamuika kuti iye?” Tsopano, Iye akutsikira ku manda. Iye anali munthu mokwanira kuti akhoza kulira; Iye anali Mulungu mokwanira kuti akhoza kuwukitsa wakufa.

130 Kuno nthawi ina kale, mkazi yemwe ali wa gulu linalake la anthu... ine ndiribe chizolowezi chomakhala ndikunena za zipembedzo. Koma mkazi uyu... Iwo samakhulupirira kuti Yesu anali Waumulungu. Iwo amati Iye anali mneneri chabe. Tsopano, Iye anali... Ngati Iye anali mneneri chabe, ife tonse tiri mu tchimo. Iye mwina anali Mulungu, panalibe chochepera kwa Mulungu, kapena wonyenga wamkulu amene dziko linayamba lakhalapo naye. Ndiko kulondola. Iye anali woposa munthu. Iye anati, “Iye sanali Waumulungu.”

131 Ziripo zochuluka kwambiri za izo mu uthenga wachitukuko uwu lero; zoyesera kuti amupange Yesu Khristu mneneri. Bwanji, Iye anali Mulungu wa aneneri. Zedidi Iye anali.

132 Iye anati, “Ine nditsimikizira izo kwa inu pogwiritsa ntchito Baibulo lanu, ‘Iye anali munthu basi.’”

133 Ine ndinati, “Inu muchite zimenezo.”

134 Ndipo iye anati, “Pamene Iye anapita ku manda a Lazaro, Baibulo limati, ‘Iye analira.’ Iye ankayenera kukhala chivundi kapena Iye sibwenzi atalira.”

135 Ine ndinati, “Dona, kodi Lemba lanu ndi limenelo?” Ine sindikutanthauza kuti ndikhale wosinjirira apa ponena izi, koma ine ndikuuzani inu zimene ine ndinamuuza iye.

136 Iye anati, “Ndi zimenezotu.”

137 Ine ndinati, “Neno limenelo ndi lofooka kuposa nsudzi wopangidwa kuchokera ku mthunzi wa nkhu ku imene yafa ndi njala.” Ine ndinati, “Chabwino, inu—inu mulibe chinthu chimodzi choti muimepo.”

138 Iye anati, “Bwanji, Iye analira. Izo zinasonyeza kuti Iye anali chivundi.”

139 Ine ndinati, “Iye anali zonse ziwiri chivundi ndi chisavundi. Iye anali Mulungu mu thupi.”

140 Iye anati, “O, zamkhutu!”

141 Ine ndinati, “Iye anapita kumanda akulira. Zimenezo zinali zoonza mokwanira, koma pamene Iye anadziwongola Yekha wamng’ono chokweza...” Baibulo limati, “Analibe zochuluka zoti ungayang’anepo pa Iye; analibe kukongola koti timukhumbire Iye.” Koma pamene Iye anawaponyera mapewa

aang'ono awo mmbuyo ndikuti, “Lazaro, dzuka,” ndipo munthu yemwe anali atafa masiku anai ndipo atavunda mmanda, iye anatulukira. Zimenezo zinali zoposa munthu. Mundisonyeze ine munthu yemwe angathe kuchita zimenezo. Chinali chiyani chimenecho? Chivundi chinamudziwa Mbuye wake. Moyo unamudziwa Mlengi wake. Chinachake chimayenera kuti chichitike. Iye analankhula ndipo munthu yemwe anali atafa ndipo atakhala mmanda masiku anai, anauka kachiwiri, ndipo anaimirira pamapazi ake, ndipo anakhala moyo. Aleluya! Ameneyo anali Mulungu mwa Mwana Wake. Inde, bwana. Ameneyo anali Mulungu akudzidziwitsa Yekha kudzera mwa Iye, Mwana. Ameneyo anali Mulungu akulankhula, osati munthu.

¹⁴² Iye anali munthu pamene Iye ankawunguza pa mtengo uja tsiku lijali akufunafuna chinachake choti adye. Amene uja anali munthu. Koma pamene Iye anatenga mabisiketi asanu ndi nsomba ziwiri ndi kudyetisa faivi sauzande, ameneyo anali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu akuwadyetsa iwo kumeneko. Iye anali woposa mneneri, woposa munthu, Iye anali Mulungu-Munthu. Zedi.

¹⁴³ Iye anagona kumbuyo kwa ngalawa yaing'ono ija usiku uja, ndipo nyanja zikukukuma ndi kumanjanja ngati chivindikiro cha pa botolo uko mu nyanja yaukali ija, pamene adierekezi teni sauzande a mu nyanja analumbirira kuti iwo amumiza Iye usiku umene uja. Iye anali munthu, wofooka ndi wotopa chifukwa cha kupempherera odwala, atagona kumbuyo uko; ndipo mphepo siimamusokoneza Iye nkomwe. Iye anali munthu pamene Iye anali akugona, koma pamene Iye anadzadzuka, nkudzaika mwendo Wake pa chingwe cha ngalawa, nayang'ana mmwamba, ndikuti, “Bata, kukhale bata,” ndipo mphepo ndi mafunde nkumumvera Iye, zimenezo anali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu mwa munthu, akudzipanga Yekha kudziwika. Ndiko kulondola.

¹⁴⁴ Iye anali munthu pa mtanda pamene Iye analira kufuna chifundo. Pamene Iye anadzalira ndi kuti, “Ine ndikuchita ludzu,” ameneyo anali munthu. Pamene Iye anafa, Iye anali munthu, koma mmawa pa Isitara pamene Iye anadzamatula zisindikizo za imfa, gehena, ndi manda, ndipo nawukanso, Iye anali woposa munthu: Zimenezo anali Mulungu akuwonetseredwa. Nzosadabwitsa wandakatulo anati:

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine; pakufa,
 Iye anandipulumutsa ine;
 Ataikidwa, Iye anandinyamulira machimo
 anga kutali;
 Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulere
 kwanthawizonse:
 Tsiku lina Iye akubwera—O, tsiku
 laulemererolo!

¹⁴⁵ Iye anati, “Chifukwa Ine ndiri moyo, inunso mudzakhala moyo. Kodi mukukhulupirira izi?” Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Kodi mukukhulupirira izi? Ine ndikukhulupirira kuti Mzimu Woyera uli pomwe pano tsopano. Kodi mukukhulupirira izi? Ine ndikukhulupirira kuti Iye atidzadza ife ndi Kukhalapo Kwake. Kodi mukukhulupirira izi? Ine ndikukhulupirira Mzimu Woyera ukufuna kuti utsanulire Kukhalapo Kwake, kuchiritsa odwala onse, kuwapanga anthu onse amene alibe Mzimu Woyera adzadzidwe. Kodi mukukhulupirira izi? Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Tiyeni tiimirire pa mapazi athu ndipo timpatse Iye matamando. Ine ndikukhulupirira Iye agwa pompano pa ife.

¹⁴⁶ O Ambuye Mulungu, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo Wamuyaya, Wopereka wa mphatso yabwino iliyonse, ife “Kodi mukukhulupirira izi,” Ambuye. Ife tikukhulupirira kuti zimenezo ndi Inu pano mu msonkhano. Ife tikukhulupirira kuti ndi Inuyo yemwe mukudalitsa miyoyo yathu. Ife tikukhulupirira kuti ndi Inuyo mukutsanulira Mzimu Wanu pa ife. Ife tikukhulupirira kuti Ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ife tikukhulupirira Ndinu wamoyo kwanthawizonse ndipo maina athu analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Miyamba yonse ndi dziko lapansi zidzapita, koma ife tidzakhala moyo kwanthawizonse, chifukwa Inu muli wamoyo kwanthawizonse. Ambuye, Inu munalonjeza izo kwa ife. Ife tikukhulupirira izo ndi mtima wathu wonse. Chirichonse chimene chiri mwa ife, ife tikukhulupirira izo, Ambuye. ine ndimamukonda Iye, Ine ndimamukonda Iye.

¹⁴⁷ Kodi inu mukumukhulupirira Iye? Ine ndikukhulupirira kuti umenewo ndi Mzimu Woyera. Pali Chinachake chimene chikugwera pa ife. Kodi mukukhulupirira izi? Ine ndikukhulupirira kuti Iye akufuna kumuchiza munthu aliyense pakali pano. Kodi mukukhulupirira izi? Kwezerani manja anu kwa Iye. Imani pa mapazi anu. Kodi mukukhulupirira izi? Mzimu Woyera uli pano. Izi ndi Zimenezo! Petro anati, “Ichi ndi Chijachi.” Ichi ndi Chimenecho, Mzimu Woyera.

¹⁴⁸ O Ambuye, Mlengi wa miyamba ndi dziko lapansi, tumizani mphamvu Yanu, ndi madalitso Anu, ndi ubwino Wanu pa anthu awa, ndipo mudalitse mitima yawo, ndipo mulole iwo awone kuti Mwana wa munthu ali wamoyo kwanthawizonse. Perekani izi, O Ambuye. Ife tikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.

¹⁴⁹ Aliyense amene alibe Mzimu Woyera, kwezani mmwamba manja anu ndipo mumutamande Mulungu. Ine ndikukhulupirira Iye agwera pa inu. Winawake ikani manja anu pa iwo. Ora lake ndi lino. Chifukwa chiyani ife tikudikiriranso? Nthawi yake ndi ino. Ino ndi nthawi ya Pentekoste, kubwerera kwa Mulungu. Yanjanani ndi Mulungu, Pentekoste! Muwulole mtima wanu ukondowedzedwe ndi mphamvu ya Mulungu

wamoyo. Mulole Mzimu Wake ubwere udzasunthire mwa inu, kudzasungunula miyoyo yanu. Iye akumakhala pano usiku ndi usiku, pano kuti adzachize odwala, kudzapereka kupenya kwa akhungu, kudzera mwa wamkulu ndi wamphamvu kwambiriyo Iye akudzitsimikizira Yekha kuti nthawizonse ndi yemweyo. Aleluya!

¹⁵⁰ Mtamandeni Iye. Kwezani manja anu. Muiwale kuti muli kuti; mungodziwa kuti mwamuzungulira Iye, ndipo ubwino Wake, ndi ulemelero Wake, ndi mphamvu Yake, ndi chifundo Chake chimapilira kwanthawizonse. Iye nthawizonse akukhalabe yemweyo. Lidalitsike Dzina la Ambuye. Aleluya! O, litamandike Dzina Lake Loyera.

¹⁵¹ O, ndi zodabwitsa bwanji, ndi wamphamvu bwanji Iye. Ndi angati amene mukufuna kuti mudzipereke miyoyo yanu kwa Mulungu pakali pano, katsopano? Kwezani mmwamba manja anu. Ndi angati mukufuna kuti mudzipereke miyoyo yanu kwa Mulungu? Ndi zimenezotu. Kwezani mmwamba manja anu. Tiyeni tiwone Pentekosite. Tiyeni tiwone anthu a Mulungu. Ine ndikweza dzanja langa. “Ambuye, ine ndiri pano. Nditumeni ine.” Mutenge Mngelo ndiye wokhala ndi makala a pa guwa ndipo mutumize mphamvu Yanu pa ife, Ambuye. Mulungu, perekani izi mu chidzalo cha Mzimu Wanu, O Atate. Imvani pemphero lathu, O Ambuye. Imvani pemphero lathu, ngati ana okhulupirira amene aimirira. Matamando akhale kwa Dzina Lake.

¹⁵² O, monga mafunde a ulemelero akugwa, o, madontho a mame a chifundo. O, Mulungu alemekezeke. Mulole miyoyo yathu idikirire. Kodi mukukhulupirira izi? Kodi mukukhulupirira izi? Uwu ndi Mzimu Woyera umene ukubwera. Iyi ndi mphamvu yosawoneka imene imatipititsa ife kukalowa mu Ufumu wa Mulungu, madalitso a Pentekoste. Kubwerera kwathu. Inu akukuyembekezerani kwanu. Ndinu anthu ofunika. Mulungu akufuna kuti inu mudzipereke nokha. Akazi, dziyeretseni nokha. Amuna, dziyeretseni nokha. Tiyeni tiwuyambepo wobwerera kwa Mulungu ndi kukamutumikira Mulungu ndi mtima woyera kwenikweni.

¹⁵³ Mulungu alemekezeke, Mzimu Woyera uli mu msonkhano. Ingochitani chimene inu mukumverera kuti muchite. Mungolola Mzimu Woyera usunthire pa inu. Palibenso chirichonse chimene ine ndinganene. Ine sindikudziwa basi chimene ndinganene tsopano. Mzimu Woyera wangokhala paliponse mchipinda muno. Lodala likhale Dzina la Ambuye. Matamando akhale kwa Ambuye. O, Aleluya! Aleluya! Matamando akhale kwa Ambuye. Ambuye alemekezeke. Ndi wodabwitsa bwanji, waulemerelo bwanji. . . Ndi wokongola bwanji, ndi kodabwitsa bwanji kupembedza kwa oyera a Mulungu pa nkhope zanu, pa Kukhalapo kwa Mzimu Woyera pano ukuyenda ndi

kutisonyezera ife ulemerelo Wake kuchokera mwa unyinji uwu mu mtima umodzi, Dzina Lake litamandike.

¹⁵⁴ Mupotoloke ndipo mugwirane chanza ndi winawake, ndikuti, “Ambuye alemekezeke, m’bale. Ambuye alemekezeke, mlongo.” Tiyeni tipite mkati momwe ndipo timulole Mulungu atikondoweze ife. Ambuye alemekezeke. Uko nkulondola. Inu nonse Amethodisti, ndi Abaptisti, ndi Apresbateria, Apentekosite, ndi a Seventh Day Adventists, ndi chirichonse chimene inu muli, mugwirane manja wina ndi mzake mu Kukhalapo kwa Ambuye Mulungu. Ndi zimenezotu. O, Aleluya! Aleluya! Aleluya! O, ndine wokondwa kwambiri ndine mmodzi wa iwo. Ndine wokondwa kwambiri. O, kugwetsera pansi makoma, kuponyera panja litsiro. Ulemerelo! Ufulu mwa Ambuye, kutamanda Dzina Lake loyera. . . Lidalitsike Dzina la Ambuye. O, Aleluya! Mulungu alemekezeke.

¹⁵⁵ O, ine ndimangokonda kuziwona zimenezo: anthu kugwirana chanza wina ndi mzake ndi kuwalitsa nkhope zawo. Mphamvu ya Mulungu ikuti, “Ndi zimenezotu. Ndi zimenezotu, ndife ana a Mulungu. Ndife tonse mpingo umodzi wawukulu, munthu mmodzi wamkulu mwa Khristu Yesu, Mkwatibwi Wake, Uyo waulemereloyo.” Kudza kwa Ambuye kukuyandikira pafupi. Anthu Ake akubwera pamodzi ndipo akudzikonda okha . . . ndi chikondi ndi mphamvu ya Kukhalapo Kwake. O, izi ziri ngati Kumwamba. O, izi ndi zabwino. Ameni. O, ndi zaulemerelo bwanji, ndi zodabwitsa bwanji: kumangompembedza Ambuye mu Mzimu ndi mu mphamvu. Nthawi yoteroyo. Polekezera pake ndi pamene . . . poyambira.

¹⁵⁶ Palibepo basi . . . ine ndinawauza abale, “Abale, palibepo malo oyimikira.” Palibepo malo apa . . . Ife sitinachite kuyamba, kotero ife sitingaima. Basi—zodabwitsa basi . . . Ndi angati akumverera bwino kwenikweni? Basi Kukhalapo kwa Ambuye, o, mai, ndi zodabwitsa, Kukhalapo kwa Ambuye apa.

¹⁵⁷ Tsopano, Kukhalapo kwa Ambuye kuli pano kuti kudzachiritse odwala, kudzawapange anthu akhale bwino. Ingomukhulupirani Iye. Kodi inu mukumukhulupirira Iye? Ngati ife tingathe mukukhulupirira Iye, zinthu zonse ndi zotheka. Inu mukukhulupirira zimenezo? Kodi mukukhulupirira kuti ndiko Kukhalapo kwa Ambuye?

¹⁵⁸ Tsopano, pamene inu . . . Ndipatseni ine mphindi chabe, mphindi chabe tsopano, ndipo tamvetserani kwa mphindi chabe. Mundirole ine nditsimikizire izo kwa inu kuti ndi Mzimu Woyera pano. Mundirole ine ndikusonyezeni inu kuti Mzimu Woyera, Uyo yemweyo amene amachita kulankhulako, Uyo yemweyo amene amachita chinthucho, akudziwa zimenezo. Ndi angati amene ali pano tsopano, amene abwera muno akudwala? Tiyeni tiwone manja anu. Iwo amene anali ndi nthenda . . . Pali anthu . . .

¹⁵⁹ Pali mwamuna amene waima apo. Kodi inu mukukhulupirira, bwana? Palibepo makadi apemphero amene aperekedwa, koma kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kukuchizani inu? Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akhoza kundiuza ine vuto lanu? Ilo liri kumbali yanu. Inu mukukonzekera oparesoni. Uko nkulondola. Dzina lanu ndi Bambo Cartwright. Uko nkulondola. Nkulondola uko? Gwedezeni dzanja lanu. Chabwino. Pitani kwanu ndipo mukakhale bwino, inu simukulisowa ilo. Inu mukukhulupirira izo?

¹⁶⁰ Bambo uyo amene wagwirizira mwana uyo mmikono yake, inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu? Inu mukukhulupirira kuti izi ndi Mzimu Woyera? Ine sindikukudziwani inu, nkulondola uko? Sindinayambe ndakuwonanipo inu mmoyo wanga; ndife alendo. Kodi mukukhulupirira Mzimu Woyera ukhoza kundiuza ine limene liri vuto ndi mwana ameneyo? Ali ndi zidzolo. Ndiko kulondola. Si kulondola kumeneko? Ndithudi. Sindinu wochokera kuno. Ayi. Inu muli ndi vuto la mmimba, limene inu mukuvutika nalo, inuyo. Ndiko kulondola, sichoncho izo? Ndinu wochokera ku Mzinda wa Kansas. Chabwino. Bwererani mmbuyo, Yesu Khristu wakuchizani inu. Aleluya! Inu mukukhulupirira. Kodi inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse?

¹⁶¹ Apa pali Mngelo wa Ambuye, wafungatira pa wamng'ono uyu—mkazi wamng'ono kwambiri uyu, wokhala ngati wachikulire, wakhala pomwe apa, akuvutika ndi thumbo. Inu mukukhulupirira Mulungu akuchizani inu kwa thumbo limenelo, mlongo? Inu, muli ndi duwa laling'ono lofiira pa chipewa chanu, kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino. Pitani kwanu ndipo mukakhale bwino. Amen. O, ndi Mulungu; ndi Khristu Mwana wa Mulungu. Iye anawuka kwa akufa. Iye ali pano.

¹⁶² Tsopano, ikanani manja pa wina ndi mzake ndipo mungopereka kanyengo kabwino ka pemphero, mmodzi aliyense wa inu, pamene ine ndikumupempha winawake kuti abwere kuno. Bwerani kuno, m'bale. Pamene inu mwaikana manja pa wina ndi mzake kuti musonyezere kuti Mulungu amachiza nayenso, ine ndiri ndi m'bale apa woti apemphere nayenso. (Teroni. Chabwino.) Matamando akhale kwa Ambuye Mulungu.



KODI MUKUKHULUPIRIRA IZI? CHA60-0402
(Believest Thou This?)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Loweruka, Epulo 2, 1960, ku Municipal Auditorium mu Tulsa, Oklahoma, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2017 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org